



**HOLY  
COMMUNION**

**MISSA  
YOYERA**

in English  
with A Service of  
Worship, Personal  
Prayers and Notes

mu Cinyanja  
ndi Mapemphero  
ndi Kupempherera ena  
ndi Cidziwitso

Diocese of Zambia

1969

## ZAMUKATIMU

Missa Yoyera ... ..	1
Mapemphero ... ..	15
Kupempherera ena ... ..	16
Mapemphero a pa masiku ... ..	19
Cidziwitso ... ..	21

# Missa Yoyera

## KUSONKHANA

*Nthawi zina angaimbe nyimbo. Pambuyo pace onse onena pamodzi ndi wansembe:*

Mlungu wamphamvuyonse, kwa inu mitima yonse yatseguka, zofuna zonse zidziwika, ndipo kulibe kanthu kobisika; Yeretsani maganizo a mitima yathu potiuzira Mzimu wanu Woyera, tikukondeni mwangwiro, ndi kulemekeza moyenera Dzina lanu loyera, mwa Kristo Ambuye wathu. Amen.

Ambuye, muticitire  
cifundo

Ambuye, muticitire  
cifundo

Ambuye, muticitire  
cifundo

Kristo, muticitire     *kapena*  
cifundo

Kristo, muticitire  
cifundo

Kristo, muticitire  
cifundo

Ambuye, muticitire  
cifundo

Ambuye, muticitire  
cifundo

Ambuye, muticitire  
cifundo

Yesu, anati, Udzikonda Ambuye Mlungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse. Ili ndilo lamulo lalikuru ndi loyamba. Ndipo laciwiri lolingana nalo ndilo, Udzikonda mnzako monga udzikonda iwe mwini. Pa malamulo awiriwa ndipo pagona cilamulo ca Ambuye ndi Aneneri.

*Anthu: Ambuye, muticitire cifundo, nimulembe malamulo awa onse m'mitima mwathu, tiku-pemphani.*

*kapena*

*M'malo mwace m'nthawi ya Lenti ndi Kudza, pa Mas. ku a sabata. Wansembe awerenge Malamulo khumi.*

1. Mlungu adanena mau awa; Ine ndine Ambuye Mlungu wako, usakhale ndi milungu ina, koma ine ndekha.

*Anthu:* **Ambuye, muticitire cifundo, ndimutembenuze mitima yathu tisunge malamulo anu.**

2. Usadzipangire wekha fano, kapena fanizo liri lonse la cinthu chakumwamba, kapena ca m'dziko lapansi, kapena ca m'madzi ndipo; usazipembedze kapena kuzitumikira.
3. Usachule Dzina la Ambuye Mlungu wako pacabe.
4. Udzikumbukira Tsiku la sabata kuti liri lopatulika. Masiku asanu ndilimodzi udzigwira nchito zako zonse kuzimariza; koma tsiku lacisanu ndi ciwiri likhale la Ambuye Mulungu wako.
5. Udzilemekeza atate ako ndi amai ako.
6. Usaphe.
7. Usacite cigololo.
8. Usabe.
9. Usanamizire.
10. Usasirire.

*Anthu:* **Ambuye muticitire cifundo ndimulembe malamulo awa m'mitima mwathu, tikupemphani.**

*Nkutheka kunena "Ulemelero" potsiriza pa Missa.*

**Ulemelero ukhale kwa Mlungu m'mwamba-mwamba, ndi mtendere panso pano, ndi kwa anthu cisomo. Tikutamandani, tikulemekezani, tikulambirani, tikukuzitsani, tikuthokozani, cifukwa ca ulemelero wanu waukuru, Ambuye Mlungu, Mfumu yakumwamba, Mlungu Atate wamphamvuyonse.**

**Ambuye, Mwana wobadwa yekha, Yesu Kristo; Ambuye Mlungu, Mwanankhosa wa Mlungu, Mwana wa Atate, Inu, wocotsa macimo a dziko, muticitire cifundo, Inu, wocotsa macimo a dziko, landirani pemphero lathu, Inu, wokhala ku dzanja lamanja la Mlungu Atate, muticitire cifundo.**

**Pakuti Inu nokha muli woyera; Inu nokha muli Ambuye; Inu nokha, Kristu, pamodzi ndi Mzimu Woyera, Muli m'mwamba-mwamba mu ulemelero wa Mlungu Atate.**

**Amen.**

- Wansembe* : Ambuye akhale ndi inu  
*Anthu* : Akhalenso ndi mzimu wanu  
*Wansembe* : Tipemphere

### **Pemphero la Tsiku**

## **MAU A MLUNGU**

### **Kalata**

*Nthawi zina angaimbe nyimbo kapena Masalimo*

- Wansembe* : Ambuye akhale ndi inu  
*Anthu* : Akhalenso ndi mzimu wanu  
*Wansembe* : Uthenga wabwino wolembedwa mu  
chapter . . . . . wa mu Uthenga wa . . . .  
kuyambila pa verse . . . . .  
*Anthu* : Ulemelero ukhale kwa Inu, Ambuye

### **Uthenga Wabino**

- Anthu* : Tikutamandani, Kristu

### **Lalikiro**

*Angate ku lalikira tsopano kapena pambuyo pa  
Cikhulupiriro*

### **Cikhulupiriro**

**Ndikhulupirira Mlungu mmodzi, Atate wampham-vuyonse, Mlengi wa kumwamba ndi dziko, Ndi zinthu zonse zooneka ndi zosaoneka: Ndi Ambuye mmodzi Yesu Kristo, Mwana wobadwa yekha wa Mlungu, Wobadwa ndi Atate, cisanalengedwe cinthu ciri conse, Mlungu wa Mlungu, Kuunika kwa Kuunika, Mlungu mwini wa Mlungu mwini, Wobadwa wosalengedwa,**

Pokhala mmodzi ndi Atate, Mwa Iye zinthu zonse zinalengedwa: Ameneyo kaamba ka ife, ndi kaamba ka cipulumutso cathu, anatsika kumwamba, Ndipo anacididwa thupi mwa Mzimu Woyera ndi Mariya Bikira, nakhala munthu, Ndipo anapacikidwira ife pamtandapo, m' nthawi ya Pontio Pilato. Nazunzidwa, naikidwa m'manda, Ndipo tsiku lacidatu anauka monga mwa malembo, Nakwera kumwamba, nakhala ku dzanja lamanja la Atate. Ndipo adzabweranso mu ulemelero kuweruza amoyo ndi akufa: Ufumu wace sudzatha.

Ndiponso ndikhulupirira Mzimu Woyera, Ambuye, Wopatsa moyo, Amene aturuka kwa Atate ndi kwa Mwana, Amene alambiridwa nakuzidwa pamodzi ndi Atate ndi Mwana, Amene analankhula mwa Anereni. Ndikhulupirira Eklezia mmodzi, Woyera, Katholiko, ndi Apostoliko. Ndibvomereza Ubatizo umodzi wokhululuka macimo. Ndipo ndilindirira Kuuka kwa akufa, Ndi moyo wa dziko lirinkudza. Amen.

## KUPELEKA

*Ngati popanda Missa osanena mau awa*

- Wansembe* : Ambuye akhale ndi inu  
*Anthu* : Akhalenso ndi mzimu wanu  
*Wansembe* : Comweco muwalitse inu kuunika kwanu pamaso pa anthu, kuti pakuona nchito zanu zabwino, alemekeze Atate Wanu wa Kumwamba.

*Kapena ngati sanena mau awa, Aimbe nyimbo pamene anthu akupeleka zopeleka, wansembe aike mkate ndi vinyo woyenera pa mazabau. Pambuyo wansembe ndi anthu anene pamodzi.*

**Ambuye tikupemphani mudalitse mphatso zanuzi, kuti zigwire nchito yoneyera, kuti zitidyetse moyo wosatha wa mzimu ndi thupi: mwa Ambuye Yesu Klistu. Amen.**

## MAPEMBEDZO

*Mkristo aliyense angathe kunena mapemphero wa kupatula lotsiriza kapena ma pemphero ena atsikulo:*

*M'tsogoleri* : Ambuye imvani pemphero lathu  
*Anthu* : Ndi kulira kwatu kukufikileni

Mlungu wamphamvuyonse, wa nthawi zosatha, mwatiphunzitsa mwa Atumwi anu oyera kupemphera ndikupembedzo, ndi kuyamika kaamba ka anthu onse: Tikupemphani modzicepetsa kulandira (zopereka zathu ndi) nsembe zathu ndi mapemphero athu tiperekaso kwa Inu. Muuzire Eklezia wanu Katoliko mzimu wa coonadi ndi cianjano. Ndi mulole kuti iwo obvomereza dzina lanu loyera ayanjane m'coonadi ca Mau anu oyera, ndi kukhala pamodzi m'cikondi canu.

Mutsogoze mitundu yonse m'njira ya cilungamo ndi mtendere. ndi kuphunzitsa Mafumu ndi Olamulira onse kuti anthu onse pakuwamvera akhale m'mtendere ndi m'kulemekeza Mlungu. Ndi mulole kuti N. President wathu, ndi nduma zace ndi nyumba ya Malamulo, ndi onse amene ali mu ulamuliro ndi alipansi pace aweruze molungama, kuletsa zoipa ndi kukhazikitsa zabwino.

Atate wakumwamba, mudalitse ma Bishopu onse, maka-maka N. Bishopu wathu, ndi Ansembe ndi otumikira onse, kuti mwa macitidwe ao ndi mau ao alalikire Mau anu, ndi kucita Masakramenti anu moyenera. Ndi mudalitse anthu onse, maka-maka iwo amene asonkhana pano, kuti timvere ndi kulandira Mau anu modzicepetsa ndi kukutumikirani moyera ndi molungama masiku onse a moyo wathu.

(Mutsogoze ndi kudalitsa onse olalikira Uthenga wabwino m'maiko onse.) (Ndi muunikire ndi Mzimu wanu masukulu onse, kuti dziko lapansi likadzale ndi cidziwitso ca coonadi canu.) (Ndi mupatse anthu onse m'maitanidwe ao osiyanasiyana akhazikitse cimvano ndi ubale pa dziko.)

Tikupemphani, Ambuye, mwa cifundo canu muthandize onse amene ali obvutika, olira, aumphawi, kapena odwala, (maka-maka . . . . .)

Tiika m'manja mwanu mwacifundo, Ambuye, atumiki anu onse amene anamwalira m'cikhulupiriro canu, (maka-maka . . . . .) nitipemphera kuti muwapatse cifundo, kuunika ndi mtendere lero ndi pa tsiku la kuuka.

Ndipo muno tikuthokozani mopambana, Ambuye, cifukwa ca ubwino wodabwitsa wa Oyera anu onse, maka-maka wa Mariya Bikira wodalitsidwa, Amai wa Mwana wanu Yesu Kristo, Ambuye wathu ndi Mlungu wathu, ndi wa Makolo Oyera, ndi Aneneri, ndi Atumwi, ndi Mboni; ndipo tikupemphani, mutipatse cisomo, kuti pokondwera m'Ciyanjano ca Oyera, titsate citsanzo cao cabwino, ndi kukhala nawo pamodzi mu ufumu wanu wakumwamba: Mutipatse ici, Atate, cifukwa ca Yesu Kristo mmodziyo, Nkhoswe ndi Mtetezi wathu.

*Anthu* : Amen



## KUKONZEKERA UKALISTIYA

Inu amene mwatembenuka ndithu kusiya macimo anu, amene mukhala m'cikondi ndi anzanu, amene mupangana kukhala ndi moyo watsopano, ndi kumvera malamulo a Mlungu, ndi kuyenda m'njira zace zoyera: bandikirani m'cikhulupiriro mulandire Sakramenti loyerali likulimbikitseni, ndi muulule kwa Mlungu wamphamvuyonse. pogwada mofatsa ndithu.

Mlungu wamphamvuyonse,  
Atate wa Ambuye wathu, Yesu  
Kristu, Mlengi wa zonse,  
Woweruza wa onse: Tibvo-  
mereza molapa macimo athu,  
amene tacita kawiri-kawiri, *kapena*  
m'maganizo ndi m'mau ndi  
m'macitidwe. Titembenuka  
mumtima ndi kumva cisoni  
cifukwa ca macimo athu-athu:  
Kuwakumbukira kuticititsa  
manyazi; mtolo wace  
ngosasenzeka. Muticitire  
cifundo, Atate wacifundo,  
Ndimutikhululukire macimo  
athu akale, Cifukwa ca Mwana  
wanu Yesu Kristu. Ambuye  
wathu: Ndimulole kuti  
kuyambira tsopano tikutumi-  
kireni bwino, ndi kukukondwere-  
tsani m'moyo watsopano,  
kucitira Dzina lanu ulemelero,  
Mwa Yesu Kristu Ambuye wathu.  
Amen.

Tiulula kwa  
Mlungu wampha-  
mvuyonse, Atate,  
ndi Mwana, ndi  
Mzimu Woyera,  
kuti tacimwa  
ndithu, m'maganizo  
ndi m'mau ndi  
m'macitidwe,  
kaamba ka kulakwa  
kwathu kwakukuru,  
Tsono tipempha  
Mlungu aticitire  
cifundo

Mlungu wamphamvuyonse, *kapena*  
Atate wakumwamba, amene  
mwa cifundo cace akhululukira  
onse otembenuka mtima ndi  
kumkhulupirira: Akucitireni  
cifundo, Akukhululukireni  
macimo anu, akupulumutseni  
ku ubwino wonse, nakufikitseni  
ku moyo wosatha, mwa Yesu  
Kristo, Ambuye wathu. AMEN.

Mlungu wampha-  
mvuyonse akuciti-  
reni cifundo,  
akukhululukireni  
macimo anu,  
akupulumutseni ku  
zoipa, akulimbiki-  
tseni mu ubwino  
wonse, nakufiki-  
tseni ku moyo  
wosatha. AMEN.

Mverani mau akulimbitsa mtima, amene Mpulumutsi  
wathu Kristo anena kwa onse omtembenukira:

Idzani kwa ine, nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo  
Ine ndidzakupumulitsani. Matt. 11.28

Mlungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa  
Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupi-  
rira Iye asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha.  
John. 3.16

Imvani zimene Paulo Woyera anena:  
Mauwa ali okhulupirika ndi oyenera konse kuti  
awalandire, kuti Kristo Yesu anadza pa dziko lapansi  
kupulumutsa ocimwa. 1 Tim. 1.15

Imvaninso zimene Yohane Woyera anena:  
Akacimwa wina, Nkhoswe tiri naye kwa Atate, ndiye  
Kristo Wolungama, ndipo Iye ndiye ciombolo ca macimo  
athu. 1 John. 2.1

## KUDARITSA

- Wansembe* : Ambuye akhale ndi inu  
*Anthu* : Akhalenso ndi mzimu wanu  
*Wansembe* : Kwezani mitima yanu  
*Anthu* : Tiikweza kwa Ambuye  
*Wansembe* : Tithokoze Ambuye Mlungu wathu  
*Anthu* : Kuli koyenera ife ndi kwabwino  
kucita cotere

*Wansembe* : Kuli koyenera kwambiri ndi kwabwino, ndi nchito yathu yofunika, kuti pa nthawi zonse ndi m'malo onse tikuthokozeni, Ambuye wapayekha, Atate wamphamvuyonse, Mlungu ku nthawi zosatha.

*(Pa nthawi dzina, pano pazanenedwa mayamiko ena a tsiku lo.)*

Cifukwa ca cimemeco, ife pamodzi ndi Angelo, ndi Angelo akuru, ndi mpingo wonse wakumwamba, tilambira ndi kulemekeza Dzina lanu lokuzika, pokutamandani nthawi zonse ndi kunena:

***Wansembe ndi Anthu: Woyera, Woyera, Woyera, Ambuye Mlungu wa makamu, Kumwamba ndi dziko kwadzala ulemelero wanu : Ulemelero ukhale kwa Inu, Ambuye wamwamba-mwamba. Wodalitsika ndi Iye amene akudza m'dzina la Ambuye. Hozanna m'mwamba-mwamba.***

*Wansembe:* Ulemelero wonse ndi ciyamiko zipatsidwe kwa Inu, Mlungu wamphamvuyonse, Atate wathu wakumwamba, cifukwa mwa cifundo canu munapereka Mwana wanu wapayekha Yesu Kristo, kuti atenge umunthu wathu ndi kufera pamtanda kudzatiombola; Ameneyo pakudzipereka yekha kamodzi, anaperekapo nsembe imodzi yokwaniratu cifukwa ca macimo a dziko lonse lapansi; ndipo anakhazikitsa cikumbutso cosalekeza ca imfa yace ya mtengo wapataru, cimene anatilamulira mu Uthenga wace woyera, ticipitirize kufikira akabweranso.

Mutimvere, Atate wacitundo, tikupemphani modzicepetesa, nimulole kuti ife olandira zolengedwa zanuza za mkate ndi vinyo, monga mwa lamulo loyera la Mpulumutsi wathu Yesu Kristo, pokumbukira imfa yace ndi mazunzo ace, tikalandire Thupi ndi Mwazi wace wodalitsika: Amene usiku uja anaperekedwa, anatenga mkate, nayamika, naunyema, napatsa ophunzira ace, nanena, TENGANI, IDYANI, ICI NDI THUPI LANGA LOPATSIDWA CIFUKWA CA INU; CITANI ICI CIKHALECIKUMBUKIRO CANGA. Koteronso citatha cakudya, analandira cikho, nayamika, napatsa iwo nanena, MUMWERE ICI INU NONSE; PAKUTI ICI NDI MWAZI WANGA WA PANGANO LATSOPANO, WOTHIRIDWA CIFUKWA CA INU, NDI ANTHU AMBIRI, KU KUCOTSA MACIMO; CITANI ICI NTHAWI ZONSE MUKAMWA, CIKHALE CIKUMBUKIRO CANGA.

Cifukwa cace, Ambuye, Atate wakumwamba, monga mwa lamulo la Mwana wanu wokondedwa, Mpulumutsi wathu Yesu Kristo, ife atumiki anu odzicepetsa, pokumbukira mazunzo ace oyera, ndi imfa yace ya mtengo wapitari ndi kuuka kwamphamvu, ndi kukwera kwace kwaulemlero, tikuthokozani mopambana cifukwa ca zokoma zambiri tinazilandira mwa iye. Ndipo poyembekeza kubweranso kwace mu mphamvu ndi mu ulemelero, tipereka kwa Inu, Mlungu wamkuru ndithu, Mkate uwu woyera wa moyo wosatha, ndi Cikho ici ca cipulumutso cacikhalire. Tikupemphani modzicepetsa kutsanyulira Mzimu wanu Woyera pa ife, ndi pa zipatso zanuza, kuti ife tonse odyerana m'Ciyanjano coyeraci, tidzale ndi cisomo canu ndi dalitso lonse lakumwamba.

Tikupemphani, Atate, mwa kukoma mtima kwanu, mulandire nsembe yathuyi, ya matamando ndi ciyamiko; nimulole mwa zoyenera zace ndi imfa yace ya Mwana

Yesu Kristo, kuti ife ndi Eklezia wanu wonse, okhulupirira mwazi wace, tikalandire cikhululukiyo ca macimo athu, ndi zokoma zina zonse za mazunzo ace. Koma tsopano, Ambuye, tadzipereka tokha kwa inu, mizimu yathu ndi matupi athu, tikhale nsembe yoyera ndi yamoyo.

Ndipo ngakhale sityenera cifukwa ca macimo athu ocuruka kukupatsani nsembe iri yonse, tikupemphani mulandire nsembe yathuyi; osawerenga zoyenera zathu koma mokhululukira macimo athu, mwa Yesu Kristo Ambuye wathu, mwa iye, ndi pamodzi ndi iye, ulemelero wonse ukhale kwa Inu. Atate wamphamvu-yonse ku nthawi zosatha.

*Anthu* : AMEN

*Wansembe* : Monga momwe Mpulumutsi wathu Yesu Kristo anatiphunzitsa, tinene molimbika mtima:

*Wansembe ndi Anthu*: ATATE WATHU wakumwamba, Dzina lanu liyereretsedwe, Ufumu wanu udze, kufuna kwanu kucitidwe, monga kumwamba, comweco pansipano. Mutipatse lero cakudya cathu calero. Mutikhululukire zocimwa zathu, monga ifenso tikhululukira oticimwira. Musatitengere kokatiyesa, koma mutipulumutse ku zoipa. Cifukwa wanu ndi ufumu, ndi mphamvu ndi ulemelero, ku nthawi zosatha. Amen.

---

(Pemphero la pamutima)

*Pakutyola mkate, mau awa aweneolwe*:

*Wansembe* : Mlendere wa Ambuye akhale ndi inu

*Anthu* : Panwdzi ndi mzimu wanu.

*Apa anene kapena aimbe*

Mwanankhosa wa Mlungu, wocotsa macimo a dziko; muticitire cifundo. (*kapena* Muwapatse mpumulo)

Mwanankhosa wa Mlungu, wocotsa macimo a dziko; muticitire cifundo. (*kapena* Muwapatse mpumulo)

Mwanankhosa wa Mlungu, wocotsa macimo a dziko; mutipatse mtendere wanu. (*kapena* muwapatse mpumulo wosatha)

---

## CIYANJANO

*Wansembe ndi Anthu* : Sityenera kuwandikira guwa lanuli, Ambuye wacifundo, pokhulupirira cilungamo cathu, koma cifundo canu cocuruka. Sityenera kutola makombo pansu pa guwa lanu. Koma Inu ndinu Ambuye wacifundo cacikhalire; Ndipo tikupemphani, Ambuye wacisomo, kuti tikadye Thupi la Mwana wanu wokonde-dwa Yesu Kristu, ndi kumwa Mwazi wace motere, kuti matupi athu amacimo ayeretsedwe ndi Thupi lace, ndi mizimu yathu itsukidwe ndi Mwazi wace wa mtengo wapatari, kuti tikhalebe mwa iye, ndi Iyenso mwa ife. Amen.

*Wansembe* : Idzani pafupi nimulandire Thupi ndi Mwazi wa Ambuye Yesu Kristo, zopatsidwa cifukwa ca inu, mumudye iye m'mitima mwanu mokhulupirira ndi moyamikira.

*Panene alikugawa mkate anene:*

Thupi la Ambuye wathu Yesu Kristo likusungeni m'thupi ndi m'mzimu kufikira moyo wosatha.

*Panene alikupereka cikho anene:*

Mwazi wa Ambuye wathu Yesu Kristo ukusungeni m'thupi ndi m'mzimu kufikira moyo wosatha.

## PEMPHERO LA PAMBUYO PA CIYANJANO

*Wansembe* : Yamikani Ambuye pakuti Iye ndiye wabwino

*Anthu* : **Pakuti cifundo cace ncosatha**

*Wansembe* : Tipemphere

Mlungu wamphamvuyonse, tikuyamikani ndi mitima yathu yonse, cifukwa mwatidyetsa cakudya ici coyera, ndico Thupi ndi Mwazi wa Mwana wanu Mpulumutsi wathu Yesu Kristo. Ndimo mutidziwitsa kuti mutikondadi ndiponso kuti tiri ziwalo zoonza za Thupi lauzimu la Mwana wanu, ndilo banja la anthu onse okhulupirika; ndi olowa Ufumu wanu, mwa zoyenera za imfa ndi mazunzo za Mwana wanu wokonedwadi. Ndipo tikupemphani modzicepetsa, Atate wakumwamba, mutithandize ndi cisomo canu, kuti tikhalebe m'ciyanjano coyeraco, ndi kuyenda monga momwe mufunira Inu, mwa Yesu Kristo Ambuye wathu, kwa iye, pamodzi ndi Inu ndi Mzimu Woyera, cilemekezo conse ndi ulemelero wonse zikhalebe ku nthawi zosatha. Amen.

*Ngati sadanena "Ulemelero" poyambira, aunene tsopano*

Ulemelero ukhale kwa Mlungu m'mwamba-mwamba, ndi mtendere pansi pano, ndi kwa anthu cisomo. Tikutama-ndani, tikulemekezani, tikulambirani, tikukuzitsani, tikuthokozani, cifukwa ca ulemelero wanu waukuru, Ambuye Mlungu, Mfumu yakumwamba, Mlungu Atate wamphamvuyonse.

Ambuye, Mwana wobadwa yekha, Yesu Kristo; Ambuye Mlungu, Mwanankhosa wa Mlungu, Mwana wa Atate, Inu, wocotsa macimo a dziko, muticitire cifundo.

Inu, wocotsa macimo a dziko, landirani pemphero lathu. Inu, wokhala ku dzanja lamanja la Mlungu Atate, muticitire cifundo.

Pakuti Inu nokha muli woyera; Inu nokha muli Ambuye; Inu nokha, Kristo, pamodzi ndi Mzimu Woyera, muli m'mwamba mu ulemelero wa Mlungu Atate. Amen.

---

## KUMWADZIKANA

*Wansembe* : Ambuye akhale ndi inu

*Anthu* : Akhalenso ndi mzimu wanu

*Wansembe* : Mukani ndi mtendere

*Anthu* : Tithokoze Mlungu

*Wansembe* : Mtendere wa Mlungu woposa

cidziwitso conse, usunge mitima yanu ndi maganizo anu kudziwa ndi kukonda Mlungu, ndi Mwana wace Yesu Kristo Ambuye wathu; ndipo dalitso la Mlungu, Atate, ndi Mwana ndi Mzimu Woyera likhalebe ndi inu ku nthawi zosatha.

*Anthu* : AMEN

*Pa Missa ya akufa pa malo pa "Dalitso", anene :*

*Wansembe* : Apumule m'mtendere

*Anthu* : Amen.



## MAPEMPHERO

---

*Mapempherowa angathe kugwiritsidwa nchito pa nthawi ili yonse imene palibe Missa. Munthu aliyense wa mu mpingo angathe kuchititsa mapempherowa mpaka pa mapeto.*

### KUSONKHANA PAMODZI

Nyimbo

Onse pamodzi anene pemphero lili pa tsamba 1

Malamulo khumi kapena malamulo awiri ali pa tsamba 1 ndi 2

Limodzi ndi mayankho ace, kuulula macimo pa tsamba 7

*Ngati Mbusa alipo, anene chikhululukiro, ngati palibe mtumiki, kapena Catechist awerenge pemphero la Trinity 21*

Ulemelero pa tsamba 2

Pemphero latsikulo

---

### PHUNZIRO

Epistola kapena Cipangano cakale

Nyimbo kapena masalimo

Evangelo

Aimbe nyimbo kapena anene Cikhulupiliro

*Zopeleka zingalandilidwe tsopano kapena pa nyimbo yotsiiza*

Lalikiro

## KUPEMPHERERA ENA

Nyimbo ingaimbidwe

Mapemphero ampingo pa tsamba 5 anganenedwe kapena mapemphero ena pa ma tsamba 19-20

*Onse anene* : Pemphero la Ambuye

Dalitso la Ambuye Yesu Kristu ndi cikondi ca Mlungu limodzi ndi cinyanjano ca Mzimu woyera zikale ndi ife tonse kunthawi zosatha. Amen.

---

## MAPEMPHERO A PA MASIKU

Mapempherowa anenedwe patsogoro pa kuika paokha monga mwa tsiku lace

---

*Tsiku la kubadwa ndi masiku a Mariamu*

Cifukwa mwatininkha Yesu Kristo, Mwana wanu wapayekha, abadwe kwa ife nthawi yino, amene mwa macitidwe a Mzimu Woyera anacitidwa munthu m'mimba ya Mariamu Bikira amai wace, wopanda banga la cimo, kuticotsera ucimo wonse.

*Epifania*

Mwa Yesu Kristo, Ambuye wathu, amene ali nalo thupi la umunthu wathu anaonetsa ulemelero wace kuti abwere nao anthu a maiko onse kuturuka mdima, alowe kuunika kwace kodabwitsa.

*Lacinai Patsogolo Pasaka*

Mwa Yesu Kristo, Ambuye wathu, amene anakonda ace lye yekha, nawakonda kufikira cimariziro, ndipo usiku ujaasanazunzidwe, anakhazikitsa zinsinsi zoyerazi, kuti ife olandira zipindulitso za Mazunzo ace ndi zamoyo za Kuuka kwace, tiyanjane ndi Umulungu wace ndi kudzala ndi cikwaniritso conse ca Mlungu.

### *Pasaka*

Koma tiyenera maka-maka kukutamandani cifukwa ca Kuuka kwaulemelo kwa Mwana wanu, Yesu Kristo, Ambuye wathu, pakuti Iye ndiye Mwanankhosa wa Pasaka weni-weni, amene anaperekedwa kaamba ka ife, natakotsa cimo la dziko, naononga imfa yace, natibwezera moyo wosatha mwa Kuuka kwace kwa akufa.

### *Tsiku la kukwera*

Mwa Mwana wanu wokonedwa Yesu Kristo, Ambuye wathu, amene atauka kwa akufa mwaulemelo, anadzionetsa yekha kwa atumwi ace onse, ndipo ali cipenyere iwo anakwera Kumwamba kutikonzera malo: kuti kumene kuli Iyeko, tikakwere ifenso ndi kukhala mu ufumu wace waulemelo.

### *Pentekote*

Mwa Yesu Kristo, Ambuye wathu, amene atakwera kumwamba-mwamba, kupyola mitambo yonse, akhala kudzanja lamanja lanu, nawapatsa Eklesia Katoliko, nthawi yino Mzimu Wanu Woyera, ndi Wopatsa moyo, kuti mwa mphamvu yace yopambana, cimwemwe ca Uthenga wa moyo wosatha ciyende ku maiko onse; nafe oturutsidwa mu mdima ndi cisokeretso, tilowe m'kuunika kweni-kweni ndi kuzindikira Inu ndi Mwana wanu, Yesu Kristo Mpulumutsi wathu.

### *Tsiku la utatu*

Amene pamodzi ndi Mwana wanu wapayeka ndi Mzimu Woyera muli Mlungu mmodzi. Ambuye mmodzi, ndinu Eni atatu koma Cikhaliidwe cimodzi; pakuti ico ticibvomera ca Ulemelo wanu, Atate, cimeneco ticibvomera ca Mwana ndi ca Mzimu Woyera, popanda kulekanitsa kapena kucepetsa.

### *Kung'azimira*

Cifukwa ca ulemelero wa Mau anu wobadwa m'thupi unawaunikira Mboni zosankhidwa pa phiri loyeralo ndi kuwaonetsa mphamvu ya ufumu wanu.

### *Oyera Onse ndi Masiku a Afumui ndi Alaliki*

Amene mwa Oyera anu mwatipatsa citsanzo ca moyo wabwino ndi cikole caulemelero ca kuitanidwa kwathu, kuti ife osungidwa nawo mtambo waukuru wotere wa mboni, tithamange mwacipiro makani athu ndi kulandira pamodzi ndi Oyerawo mphoto ya ulemelero yosafota.

### *Kwa Akufa*

Mwa Yesu Kristo, Ambuye wathu, amene atipatsa cikhulupiro ca kuuka akufa kwa ulemelero, kuti anthu omwe olira-lira cifukwa imfa iwafikira adzitonhoze okha, ndi cibvomerezo cija ca moyo wosatha. Pakuti kwa anthu anu okhulupirika, Ambuye, moyo udzasandulika, wosacotsedwai, ndipo pamene msasa wa thupi lathu ugwetsedwa, tiri nayo nyumba yosatha Kumwamba.

### *Cikumbukiro ca kanisa*

Amene ngakhale Kumwamba-mwamba sikukufikirani, ndipo ulemelero wanu uli m'dziko lonse, mulole kuwadalitsa malo okuyembekezani ndi momwemo muwapatsa anthu anu okhulupirika mphoto za cisomo canu.

## MAPEMPHERO ENA

### 1. *Asanalandire Ukalistia*

Ambuye, Ndibwera kwa inu cifukwa mundiitana  
Ndibwera kukutokozani cifukwa ca cikondi canu  
cacikuru

Ndibwera kupeleka moyo wanga wonse kwa inu  
kupempha cikhululukidwe ca zonse zosayenera  
kupempha kuti ndikhale watsopanonso m'kukutumikilani

Ambuye, Ndibwera pamodzi ndi Akristo anzanga onse  
Kwezani mitima yathu kuti tikhale ndi inu

Mutidzadze ndi moyo wanu wosatha

kuti tikhale tonse ndi inu m'modzi

Musaklamenti ili la Ukalistia.

### 2. *Pambuyo pa kulandira Ukalistia*

Ambuye, tikutokozani

Kumbukilani, Ambuye, izo munaticitira mu mitima  
yathu, koma osati zimene tiyenera ife, ndi m'mene  
mwatiitana kukutumikilani, mutikonze kuti tikhale  
oyenera kuitanidwa, cifukwa ca Yesu Kristo. Amen.

### 3. *M'mawa mulimonse*

Ambuye, ndizipeleka kwa inu lero,

Nditengeni, Ambuye, ndi kundigwilisila ncito zanu.

### 4. *Pa nthawi zonse*

Kristo alibe thupi pansi pano nthawi zino, koma thupi  
lathu

Alibe manja koma manja athu, alibe myendo koma  
myendo yathu,

Maso athu ndi m'mene cifundo ca Kristo

Chimayang'ila dziko la pansi pano,

Yathu ndi myendo Kristo angayendelako pocita za-  
bwino.

Athu ndi manja amene angadalitseko anthu tsopano.

5. *Mulungu Atamandike*

Titamande Mlungu.

Titamande dzina lace loyera-yera.

Titamande Yesu Kristo, Mlungu ndi munthu pamodzi.

Titamande dzina la Yesu

Titamande Yesu m'Sakramenti loyera

Titamande Mlungu Mzimu Woyera

Titamande Maria, Virgo ndi amai

Titamande Mlungu mwa Anjelo ndi Oyera ace onse

Titamande Mlungu.

6. *Pemphero la Africa*

Mlungu dalitsani Africa

Cinjilidzani anthu ace

Tsogololelani atsogoleri ace

Muapatse mtendere

Cifukwa ca Yesu Kristo. Amen.

7. *Pemphero la Zambia*

Mlungu, Atate a anthu onse, tikupemphani muapatse

anthu a dziko lino mtima wa cilungamo, zoonu ndi

cikondi, kuti m'zonse zimene ticita wina ndi mzace,

angalangidze ubale muli inu, cifukwa ca Yesu Kristo

Ambuye athu. Amen.

8. *Pemphero la Krisostom Oyera*

Mlungu wa mphamvu zonse, mwapatsa tsopano

cisomo kuti tipemphere ndi mtima umodzi kwa inu,

ndipo mumapangana kuti pamene pali awiri kapena

atatu asonkhana m'dzina lanu mungawapatse zimene

adzipempha. Kwanitsani, Ambuye, mafunilo ndi

mapemphero a atumiki anu, zingakhale zabwino kwa

iu; mutipatse m'dziko lino la pansu kudziwa zoonu

zanu, ndi m'dziko limene libwera moyo wosatha. Amen.

## CIDZIWITSO

1. 'Ulemelero' mungasiye pa masiku a Mlungu, masiku a Advent ndi kucokera pa Septuagesima mpaka Tsiku la Kanjeza, ndiponso pa masiku amene sali masiku akuru.
2. Ndicobvomeredzeka kunena pemphero (collect) limodzi lokha.
3. Pamene mkalibe kunena kapena kuimba Epistola munganene mau ocokera mu Cipangano Cakale, salimo kapena canticle. Mkristo aliyense angawerenge Epistola.
4. Pa masiku amene sali akuru Cikhulupiriro mungathe kusiya, osakamba.
5. Mapembedzo angakambidwe ndi Mkristo aliyense. Wokambayo anganene mapemphero a mu 1964 Liturgy, angaonjezepo mapemphero ena pa kufuna kwache kapena mapemphero olembedwa m'buku ili.
6. Pa masiku ena, osati pa Tsiku la Mlungu, mungathe kuleka mau ochulidwa 'Kudzikonzera'. Pa tsiku lililonse mungakambe mau a Kuulula ndi Cikhulukiro atali kapena afupi m'mene mungafunile ndiponso mungathe kuleka mau Olimbitsa Mtima.
7. Mungaimbe kapena kunena 'Mwanankhosa' wa Mlungu' pa nthawi ya kulandila Ukalistia kapena atamaliza kudula mkate.
8. Pa kulandiritsa Ukalistia mau okambidwa angathe kucepetsako ndi kunena motele:  
Thupi ka Kristu. *Amen.* Mwazi wa Kristu. *Amen.*

## CONTENTS

Holy Communion	...	...	...	...	...	...	1
Service of Worship	...	...	...	...	...	...	15
Special Thanksgivings	...	...	...	...	...	...	16
Personal Prayers	...	...	...	...	...	...	19
Notes	...	...	...	...	...	...	21



# Holy Communion

## THE GATHERING TOGETHER

*A hymn may be sung. All then say with the priest:*

ALMIGHTY GOD, unto whom all hearts are open, all desires known and from whom no secrets are hid :  
Cleanse the thoughts of our hearts by the inspiration of thy Holy Spirit, that we may perfectly love thee and worthily magnify thy Holy Name ; through Jesus Christ our Lord. Amen.

Lord have mercy  
**Lord have mercy**  
Lord have mercy  
**Christ have mercy**  
Christ have mercy *or*  
**Christ have mercy**  
Lord have mercy  
**Lord have mercy**  
Lord have mercy

Jesus said : Thou shalt love the Lord thy God with all thy heart, and with all thy soul, and with all thy mind. This is the first and great commandment. And the second is like unto it. Thou shalt love thy neighbour as thyself. On these two commandments hang all the law and the prophets.

*People : Lord have mercy upon us and write these thy laws in our hearts, we beseech thee.*

*or*

*On the Sundays of Advent and Lent and on other occasions, the ten commandments may be said instead.*

1. God spoke these words saying : I am the Lord your God; you shall have no other gods before me.

*People* : **Lord have mercy upon us and incline our hearts to keep this law.**

2. You shall not make yourself a graven image, or any likeness of any thing that is in heaven above, or that is in the earth beneath, or that is in the water under the earth. You shall not bow down to them, or serve them.

3. You shall not take the name of the Lord your God in vain.

4. Remember the Sabbath day, to keep it holy.

5. Honour your father and your mother.

6. You shall not kill.

7. You shall not commit adultery.

8. You shall not steal.

9. You shall not bear false witness against your neighbour.

10. You shall not covet.

*People*: **Lord have mercy upon us and write these thy laws in our hearts, we beseech thee.**

*The Gloria may come here or at the end of the service.*

**Glory be to God on high**, and in earth peace, good will towards men. We praise thee, we bless thee, we worship thee, we glorify thee, we give thanks to thee for thy great glory, O Lord God, heavenly King, God the Father Almighty.

